


UTHENGA WABWINO WA CHOONADI

Malangizo ndi Chilimbikitso
kuchokera m'Baibulo kupita kwa
amene akulalikira Uthenga Wabwino

ZINA ZOTENGEDWA KUCHOKERA KU MBIRI YA CHIKHRISTU ZOKHUDZA MAIMBIDWE A A CAPPELLA MU CHIPEMBEDZO CHAUZIMU



by Harlan Sorrell

Kuimba kogwiritsa ntchito zida sikunayambe mu chipembedzo cha Chikristu kufikira mpaka pa nthawi imene mpingo wa Chikatolika unayamba kuchita zachinyengo, komabe ngakhale nthawi imeneyo, mpingo wa Chikatolika unavomereza izi ndi mtima umodzi. Mpingo wa Greek Orthodox sunavomereze nkomwe kupembedza kogwiritsa ntchito zida, ndipo ndi zoonekeratu kuti okonzanso mpingo a Chiprotestant anachotsa zida pa chipembedzo.

Mau akuti *a cappella* ndi mau a Chilatini, amene amachokera ku mau ena awiri, *a* kutanthauza “malingana ndi” ndipo *cappella* kutanthauza “tchalichi”. Dictionary ya Webster imanena kuti *a cappella* ndi “Machitidwe a nyimbo za mu tchalichi, makamaka zakale, zimene zilibe chida chothandizira.” Mbiri yakale ikunena ndithu kuti amenewa anali machitidwe a maimbidwe a mu mpingo kuchokera mu masiku a Atumwi.

Mlaliki wakale wa mpingo wa Baptist wodziwika bwino dzina lake Charles Spurgeon, ananapo molunjika ndi moona ndithu pamene anati zida zoimbira “zimangotchinga kuposana ndi kuthandizira malemekezo athu.” Nyimbo zokometsetsa zimene zimamveka padziko pano ndiwo mau a oyera mtima osakaniza ndi mingoli yanthetemya pamene akuimba motsogozedwa ndi Mzimu. Maimbidwe oterewa ali

ndi chikoka cha kumwamba chimene chimatakasa iwo oyera mu mtima komanso kupereka chidwi kwa anthu ochimwa.

Onse amene amawerenga mozama Malemba komanso mbiri ya mpingo amadziwa chifukwa chimene mpingo wa Atumwi sunagwiritse ntchito zida zoimbira komanso iwo amene amabatizanso (Anabaptists) ngakhale okonzanso mpingo monga Martin Luther, John Wesley, ndi ena ambiri kuphatikiza D. S. Warner, anakana kugwiritsa ntchito zida mu chipembedzo cha uzimu. Iwo anagwiritsa ntchito zida zoimbira kuti zithandizire kupeka nyimbo zimene iwo analemba, kapena pofuna kudzisangalatsa kapena pa masangalalo a gulu, koma anakana kuzigwiritsa ntchito mu *chipembedzo* chifukwa anazindikira mfundo zimene zikuphunzitsidwa pa Yohane 4:23-24 ndi pa Machitidwe 17:24-25, etc. Kwa iwowo, kupembedza kunali kudzikhuthula kwa *munthu wamkati*, kaya ndi popemphera, kulalikira ndi mu nyimbo. Zida zoimbira zimatengedwa kuti sizoyenera kuti zidzigwira ntchito mu chipembedzo chauzimu. Monga mmene mbiri ikunenera ponena za Akhristu akale, iwo “anali auzimu kwambiri kuti sakanatha kumagwiritsa ntchito zida zoimbira zimene zili zopanda moyo kuti zithandizire kapena kulowa mmalo mwa liu la munthu” (*Catholic Encyclopedia*. X, 651). Palibenso maimbidwe ena okoma padziko pano kuposa kulumikizana kwa mau a anthu amene akuimba mogwirizana m'magawo onse anai a sapurano, tina, oloto ndi besi. Tsoka ilo, unyinjwa wa anthu masiku ano sunakhale ndi mwai

(Yapitirira pa tsamba 2)

“Maimbidwe okometsetsa amene anamvekako padziko lino ndiwo mau a oyera mtima ophatikizana ndi kaimbidwe kokoma ndikolemerera pamene akuimba mu Mzimu.”



ZIMENE BAIBULO LIMAPHUNZITSA ZA...

Mau a Mulungu

2 Tim. 3:16-17; 2 Pet. 1:20-21; Mat. 24:35

Ubale wa Chikondi

Mat. 22:37-40; Yoh. 14:21-23; 1 Yoh. 4:7-11

Kulapa

Mach. 3:19; Mach. 17:30; 2 Akor. 7:10

Kubadwa mwatsopano

Yoh. 3:3-7; 2 Akor. 5:17; Aro. 6:1-4;
Aef. 2:1, 5-6

Kupulumuka ku uchimo

1 Yoh. 5:18; Mat. 1:21; Yoh. 8:11

Chidzalo cha Mzimu Woyera

Mach. 19:2; Mach. 15:8-9; Mach. 1:8

Chiyero

Luk. 1:73-75; Aheb. 12:14; 1 Pet. 1:15-16;
Tit. 2:11-12; Aro. 6:22

Ufumu wa Mulungu

Luk. 17:20-21; Aro. 14:17; Yoh. 18:36

Mpingo

Mach. 2:47; Aef. 4:4-6; 1 Akor. 12:12-13;
Akol. 1:18

Umodzi

Yoh. 17:20-23; Agal. 3:28; Chiv. 18:2-4

Maskaramenti

Mat. 28:19-20; Mat. 26:26-30;
1 Akor. 11:23-27; Yoh. 13:14-17

Machiritso

Luk. 4:18; Yes. 53:4-5; Yak. 5:13-16

Chiyero cha Banja

Mat. 19:5-6; Luk. 16:18; Aro. 7:2-3;
1 Akor. 7:10-11

Chikhalidwe cha pakati pa anthu ena

1 Tim. 2:9-10; 1 Akor. 11:14-15; Deut. 22:5

Masiku omaliza

2 Pet. 3:7-12; Yoh. 5:28-29; 2 Akor. 5:10;
Mat. 25:31-46

Kukhala mwa mtendere

Luk. 6:27-29; Luk. 18:20

Kupembedza

Yoh. 4:23-24; Aef. 5:19; 2 Akor. 3:17

Kulalikira Uthenga Wabwino

Mrk. 16:15

(Kuchokera pa tsamba 1)

wakumva maimbidwe okoma ndi osowa akumwambawa. Maimbidwewa amagwira mtima ndi kutsitsimutsa moyo koposa china chonse.

Mu nyengo ino, kupembedza kovomerezeka ndi koono kumachitika pamene anthu akwezedwa kuti akhale ndi Khristu m'miyamba mu Mzimu. Kupembedza kotereku sikungakhale kwa mwambo chabe kapena kochitika ndi thupi koma kumachitika pamene mzimu wa munthu walumikizana ndi mzimu wa Kumwamba. Timaimba, kupemphera ndi kunenera (kulalikira) mu Mzimu, pokhala ndi ulamuliro wa mu Chipangano Chatsopano kuti tikhoza kuphatikiza zonsezi mu chipembedzo chathu. Komatu sitipeza pamene akupereka lamulo la *kusewera* mu Mzimu. Mzimu Woyera amadzoza maimbidwe okhawo amene amachokera mkatikati mwa mtima ndi moyo wa munthu. Mulungu alibe chidwi kapena kukondwa ndi maimbidwe athu ochokera ku zida zoimbira. Iye amafunitsitsa kumva nthetemya ndi kununkhiza fungo lonunkhira la mingoli ya mitima yathu.

Ndiye pali iwo amene amaganiza kuti kuchotsa zida zoimbira pa chipembedzo kukhoza kusulutsa kulemerera kwa chipembedzochi. Izi sizili choncho ngati zipembedzozo zikutsogozedwa ndi Mzimu Woyera. Kulemerera kwa mwambo wa chipembedzo kumalimbikitsidwa pamene zida zoimbira zachotsedwa ndipo mwambowo ungokhala chidzalo cha chiyanjano chazimu pakati pa mizimu ya opembedzawo nd Mzimu wa Mulungu. Ndi pamenepo pomwe timafika pokumva liu limene Mulungu amakondweretsedwa atalimva—la nthetemya ndi kulumikizana limene limakwera kuchokera m'mitima imene yalumikizana ndi Mzimu wake ndipo ikuimba ndi mingoli ya moyo wakumwamba ndi yaulemerero. Mulungu sanachotse zolamulira ndi miyamba ya Chipangano Chakale ndi kutisiyira chinthu chopepuka. Iye anatipatsa chinthu chabwino koposa!

Maimbidwe a a cappella mu chipembedzo chakumwamba asamatengedwe ngati kuti ndi kukakamiza, koma ndi chinthu cha mtengo wapatali chimene tachilandira kuchokera m'masiku oyeretsetsa a Chikhristu choyambirira.

“Ambuye poyamba anakhala mu akachisi opangidwa ndi manja a anthu, Ndipo anali ndi anthu amodzi, gulu losankhika la Israele; Ndipo pa Yerusalemu, mu njira za malamulo, [D. O. Teasley] Anapembedzedwa ndi olungama a masiku akale.”

Koma Mulungu anali ndi zinthu zabwino kuposa zimene anatisungira, Pamene malamulo akale adzakhale opanda ntchito [Ahebri 9:10], Ndipo Iye adzakhala mkati mwa matupi a anthu, ndipo kupembedza kudzakhala nsembe ya mitima yathu.



Gospel Truth ndi kalata imene imasindikizidwa miyezi itatu iliyonse ndi a mpingo wa Church of God pofuna kulangiza ndi kulimbikitsa zoonadi zopezeka mu Baibulo. Kutimudziwe zambiri werengani pa intaneti popita pa www.thegospeltruth.org ndipo muyankhe email imene mulandire ngati mukufuna kuti mudzilandira nawo kalatayi. Kalata ya *Gospel Truth* imasindikizidwa mu maiko ambiri kuti iperekedwe kwaulere m'dzikomo ndipo chuma chothandizira ntchitoyi chimachokera ku ndalama zimene ena amapereka mwaufulu. Ngati mukufuna lisiti yoonetsa zimene mwapereka, tidzakupatsani.

—Editor, Michael Smith

Gospel Truth, P.O. Box 2042, Nixa, MO 65714 USA
editor@thegospeltruth.org

Mau a Mkonzi



Perekani kwa Yehova ulemerero wa dzina lake, gwadirani Yehova moyera ndi mokometsetsa.—Masalmo 29:2

Ulendo uno tipitirizanso kukambirana zimene tinayambapo pamene tinayala maziko mu Kalata 18 yokhudzana ndi mapangano awiri amene Mulungu anakhazikitsa. Anthu a Mulungu samutumikiranso mwa thupi koma motsogozedwa ndi Mzimu. Kugwiritsa ntchito zida zoimbira pa nthawi ya chipembedzo sikupezeka mu mpingo wa mu Chipangano Chatsopano. Kulira kochokera mu zida izi zopanda moyo sikumabweretsa ulemerero wapadera kwa Mulungu pa chipembedzo koposa mmene kumachitira kuyatsa makandulo pa nthawi ya chipembedzo. Mulungu amalemekezedwa ndi zonedwa pakamwa kuchokera mu mtima woona ndi woyera. Anthu ambiri amanena kuti nkhani iyi ndi yosafunikira ndipo tikhoza kuzichita kapena kusachita. Kodi ndiye kuti tidzifukiza nsembe kapenanso kutsatira zitsanzo zina ka kapembedzedwe mu Chipangano Chakale? Chipangano Chatsopano sichinaletse kapena kuvomereza miyambo iyi chifukwa iyo inaposedwa ndi kupembedza kwa uzimu. Pamene zinthu zili bwino, kugwiritsa ntchito zida zoimbira mu chipembedzo sikulimbikitsidwa.

Ndakhala mu zipembedzo zambiri ku Amerika ndi maiko ena kumene anthu anagwiritsa ntchito zida zoimbira ngati gawo limodzi la chipembedzo chawo. Ngakhale kuti izi zinasangalatsa thupi nthawi zina, ndikadafunabe nditadziwa ngati izi zinawonjezera ku chipembedzo chawo chinthu chauzimu chaphindu. Mmalowake, pakati pa anthu amene amaoneka kuti ali ndi mtima weniweni pa Mulungu, ndinapeza kuti zida zoimbira zinali ngati chotchinga ku kuyenda momasuka kwa Mzimu wa Mulungu pakati pawo. Tikatengera ku gawo la maimbidwe, mipingo ina yaing'ono ikhoza kufuna kugwiritsa ntchito piano kapena zida zina pofuna kuthandizira maimbidwe awo. Nkwabwino kupembedza ndi milomo yathu ngati chopereka mmalo mogwiritsa ntchito zida monga mmene Mau amatilamulira.

Anthu ambiri amakira kumbuyo mchitidwe wogwiritsa ntchito zida mu chipembedzo ponena kuti ndi chikhalidwe chawo. Ngakhale kuti kuimba ng'oma kapena piano chikhoza kukhala chikhalidwe chimene anthu amachikonda, sizitenga nthawi kuti tizindikire kuti chisangalalocho ndi cha kuthupi basi.

Ena amanena kuti miyoyo idzakokedwa ku zipembedzo ndi kupulumutsidwa kuti ibwere kwa Ambuye ngati tagwiritsa ntchito zida zoimbira. Izi zikungowonetseratu kuti pali kusamvetsetsa pa zinthu zauzimu. Yohane 6:43-44 akunena kuti “Kulibe mmodzi akhoza kudza kwa Ine koma ngati Atate wondituma Ine amkoka iye.” Chimene chimatipangitsa kuti tiwakoke anthu ndi chinthu chimene tikuwakokeracho. Ngati tigwiritsa ntchito njira za thupi pofuna kukoka ndi kutakasa anthu, tidzayenera kupitiriza kugwiritsa ntchito njira za thupi kuti tiwasangalatse apo ayi adzatithawa. Mzimu Woyera akufuna kuti ayale maziko ndi kutsogolera koma ndi Mzimu yekha amene angabweretse kulapa kwa umulungu ndiponso kukhudza mtima wa munthu.

Maimbidwe ndi ake a Ambuye ndipo ndi mphatso yodabwitsa kwa anthu. Anthu a Mulungu akulangizidwa kuti *aimbe* polemekeza Mulungu ndi kulimbikitsana wina ndi mnzake. Zida zoimbira zikhoza kukhala mlowammalo wosavuta wa kudzoza kwenikweni ndi kuyenda kwa Mzimu wa Mulungu. Ngati Mzimu wa Mulungu sakudzoza mwambo wa chipembedzo, mwambowo ndi wozizira ndi wakufa. Popanda Mzimu, sizodabwitsa kuti anthu amafuna kwambiri zida zoimbira kuti zikwaniritse chimene chikusowa – kuti akhoza kuimba bwino motani potsogozedwa ndi Mzimu pamene akuphunzitsidwa ndi Mau komanso mmene umachitira mpingo woyamba. Kuimba kopanda zida ndi “njira yabwino kwambiri” ndipo chinthu chimene anthu a Mulungu akuyenera kumachita.

Michael W. Smith

July 2017

Zambiri Zili pa
INTANETI

Mukafuna kutipeza

pa intaneti, mulembe

www.thegospeltruth.org

kuti mudzilandira makalata

athu kapenanso kuti

muone makalata akale.



Mitundu ndi zizindikiro

za zida zoimbira

Ndi chinthu chosangalatsa kwambiri pamene tilingalira za zida zoimbira ngati mitundu ndi zizindikiro za umodzi umene Mzimu Woyera amabweretsa m'miyoyo ya anthu a Mulungu. Pamene kachisi wa Solomoni anapatulidwa, ansembe okwana 120 anaomba malipenga pamodzi ndi oimba pofuna kulemekeza ndi kuyamika Mulungu (2 Mbiri 5:12-14). Ulemerero wa Mulungu unatsika ndipo unadzaza kachisiyo. Mu Chipangano Chatsopano, pa tsiku la Pentekoste, otsatira a Khristu okwana 120 anali mu chipinda chapamwamba mu mtima umodzi. Mzimu Woyera anatsika pa iwo ndi kuwadzaza ndi ulemerero wake. Kenaka iwo anakhala zida za chilungamo pofuna kuchita chifuniro cha Mulungu.

Kalozera posanthula Mau a Mulungu

Mutu: Maimbidwe mu chipembedzo

Kuwerenga Mau a Mulungu: *Koma ikudza nthawi, ndipo tsopano ilipo, imene olambira oona adzalambira Atate mumzimu ndi m'choonadi; pakuti Atate afuna otere akhale olambira ake. Mulungu ndiye mzimu; ndipo omlambira lye ayenera kumlambira mumzimu ndi m'choonadi. —Yohane 4:23-24*

Mwachidule: Zida zoimbira zimagwiritsidwa ntchito mu Chipangano Chakale pamene kutumikira Mulungu kumakhazikika pa miyambo ndi machitidwe a thupi. Chipembedzo mu nyengo ya mu Chipangano Chatsopano chikuyenera kukhala cha Mzimu ndipo Mulungu akulangiza anthu Ake kuti *aimbe* osati *kusewera*. Maimbidwe ongowiritsa ntchito pakamwa osati zida ndiwo mulingo ndi machitidwe a mpingo wa Mulungu.

I. Zida zoimbira mu Chipangano Chakale

- A. Genesis 4:21 Zinapangidwa koyamba ndi Yubala.
- B. Mlaliki 2:8 Zimasangalatsa ana a anthu.
- C. Eksodo 15:20-21 Miriamu anaimbira zida.
- D. 2 Mbiri 20:27-28 Zimagwiritsidwa ntchito pokondwerera chipambano.
- E. 1 Samuele 10:5 Aneneri amatumikira mothandizidwa ndi zida.

II. Mfumu Davide ndi zida zoimbira

- A. 1 Samuele 16:15-23 Anali katswiri wa woimba zida. Akaimba mzimu woipa umachoka mwa Saulo.
- B. Masalmo 33:1-3 Lemekezani ndi zida. (Masalmo 150:1-6)
- C. 1 Mbiri 15:15-16 Davide analamulira kugwiritsa ntchito zida.

III. Zida pa chipembedzo cha m'Kachisi monga lamulo la Davide

- A. 1 Mbiri 23:5 Davide apanga zida zogwiritsa ntchito mu Kachisi. (2 Mbiri 5:1)
- B. 1 Mbiri 25:6 Zida malingana ndi lamulo la Davide.
- C. 2 Mbiri 29:25-28 Analamula ndipo zinagwira ntchito monga ananenera Davide. (Ezara 3:10)

IV. Kudzudzula kwa aneneri

- A. Yesaya 5:11-13 Maimbidwe amagwiritsidwa ntchito pa maphwando a kuthupi.
- B. Amosi 6:1-5 Tsoka likunenedwa pa iwo amene apanga zida ngati za Davide. (Amosi 5:21-24)

V. Muyeso watsopano mu nyengo ya Chipangano Chatsopano

- A. Mateyu 5:17 Lamulo likwaniritsidwa.
- B. Ahebri 10:1-9 Muyeso watsopano.
- C. Yohane 4:23-24 Opembedza enieni amapembedza mu mzimu ndi mu choonadi.
- D. Machitidwe 17:22-25 Mulungu salambiridwa ndi manja a anthu.

VI. Chiphunzitso ndi mchitidwe mu Chipangano Chatsopano

- A. Mateyu 26:30 Yesu ndi ophunzira ake anaimba nyimbo.
- B. Aroma 15:9 Imbani kuti mulemekeze Mulungu.
- C. 1 Akorinto 14:15 Imbani ndi mzimu ndi chidziwitso.
- D. Aefeso 5:18-20 Imbani ndi kuthira mang'ombe mu mtima.
- E. Akolose 3:16 Imbani Masalmo, mayamiko, ndi nyimbo zina zauzimu. (Yakobo 5:13)
- F. Ahebri 2:12 Imbani zoyamika.
- G. Ahebri 13:15 Perekani nsembe za mayamiko kuchokera pa milomo.

VII. Kupembedza kwa dziko lapansi

- A. 2 Timoteo 3:1-5 Okonda zosangalatsa thupi.
- B. 1 Yohane 2:15-17 Musakonde dziko lapansi.

VIII. Kupembedza kwauzimu

- A. Aroma 12:1-2 Musafanizidwe ndi machitidwe a pansi pano.
- B. 1 Petro 2:5 Perekani nsembe zauzimu.

Kumaliza: *Ndi kuphunzitsa ndi kuimbirana eni okha ndi masalmo, ndi mayamiko ndi nyimbo zauzimu, ndi kuimbira Mulungu ndi chisomo mumtima mwanu. —Akolose 3:16*



Maimbidwe MU CHIPEMBEDZO

“Koma ikudza nthawi, ndipo tsopano ilipo, imene olambira oona adzalambira Atate mumzimu ndi m’choonadi; pakuti Atate afuna otere akhale olambira ake” (Yohane 4:23). Yesu analankhula motero kwa mzimai wa Chisamariya pa chitsime paja. Mau a Khristu anaonetseratu mwamvemvemve kuti kusintha kunali kutafika ndipo machitidwe ndi chikhalidwe cha kupembedza kwenikweni zidzakhala zosiyana.

Kupembedza kwenikweni kukufunikira

Mu nyengo imene inalipo Khristu asanabwere, kulambira kumachitika mongotsatira chipembedzo komanso mwa mwambo. Anthu a Mulungu amasunga masiku ena kukhala opatulika, ndipo amapereka nsembe, nafukiza, ndi kutsata miyambo ya kusamba m’manja, kuimba nyimbo pa chipembedzo pogwiritsa ntchito zida, ndi zina zotere. Chifukwa cha kubwera kwa Khristu, Mulungu sanakhutitsidwenso ndi kupembedza kongogwiritsa ntchito thupi koma anasangalatsidwa ndi chiyanjano cha uzimu kuchokera mu mtima wa munthu kudzera mu kupezeka kwa Mzimu Woyera. Ngakhale kuti kupembedza konyenga kukupitirirabe, masiku ano Mulungu akufunabe anthu opembedza moona.

Gawo lalikulu la chipembedzo mu Chikhristu cha masiku ano lagona pa kugwiritsa ntchito zida zoimbira. Chidzikhala chikhumbokhumbo cha ana a Mulungu kukhala “Opembedza oona” ndi kuchita mwanjira imene ikhoza kukhala chiyero ndipo imene ibweretse ulemu, kulemekeza ndi kukuza Mulungu kwakukulu. Nthawi ya

chipembedzo idzikhala nthawi imene tipereka ulemero kwa Mulungu ndipo idzikhala imene gulu la okhulupirira limalimbikitsana mu uzimu. Ndi cholinga chimenecho m’maganizo ndi mumtima mwathu, kodi Mulungu akhoza kulambiridwa bwinobwino ndi zida zoimbira?

Pali zinthu zambiri zimene Mulungu sanazinene tchutchutchu mu Baibulo, koma Iye anatisiyira mfundo zoonadi kuti tizitsatire. Tikatenga zimene zinachitika mu mbiri ya mpingo ndi kuphatikizapo ndi zimene zikuchitika panopa, nzowonekeratu kuti kudzera mu Mau ndi Mzimu, kugwiritsa ntchito zida zoimbira sikuthandizira kukuza kupembedza kwa muuzimu mu nyengo ino ya chisomo.

Chiyambi cha zida zoimbira

Mu Genesis 4:21 timamva za Yubala, chidzukululu cha Kaini, amene anali “atate wao wa iwo oimba zeze ndi chitoliro.” M’malemba, zidzukululu za Kaini zimatchedwa kuti “ana aamuna a anthu” chifukwa iwo sanatsatire malamulo a Mulungu monga zinachitira zidzukululu zina za Seti zotchedwa “ana aamuna a Mulungu.” Ndi zosangalatsa kuti zida zonse zoimbira zinapangidwa ndi anthu osaopa Mulungu amene analibe cholinga chilichonse chofuna kukondweretsa Mulungu. Ngakhale kuti zida zoimbira sizolakwika kuzigwiritsa ntchito pa zolinga zina ndi zochitika zina, mdaniyo wazigwiritsa ntchito kumibadwomibadwo pofuna kuwachotsa anthu pa Iye amene angatumikire mtima wao moonadi komanso kuwapatsa mtendere weniweni wa mumtima. Solomononi anachitira umboni za kusonkhetsa pamodzi golide, siliva, oimba pamene anati: “ndinaitanitsa amuna ndi akazi akuimba ndi zokondweretsazo za ana a anthu, ndizo zoimbira za mitundumitundu” (Mlaliki 2:8); komabe pamapeto pake anavomereza kuti zonsezo zinali “zachabechebe ndi kungosautsa mtima” (2:11). Ngakhale kuti kulira kwa zida zoimbira kukhoza kusangalatsa, kuthunzitsa ndi kupoletsa pang’ono mavuto a mtima, sikunakwanitse kufika pobweretsa chiyero.

(Yapitirira pa tsamba 6)

Kagwiritsidwe ntchito ka zida mu Chipangano Chakale

Zida zoimbira zimagwiritsidwa ntchito mu njira zosiyanasiyana ndi anthu a Mulungu a mu Chipangano Chakale. Ataoloka Nyanja Yofiira, Miriyamu, mlongo wake wa Aroni, anatenga lingaka m'dzanja lake ndipo anavina ndi azimai ena (Eksodo 15:20-21) mu njira yogwedeza thupi posonyeza kukondwa kwawo ndi kupereka mayamiko kwa Ambuye. Zida zoimbira zimagwiritsidwa ntchito pamene apambana kunkhondo (2 Mbiri 20:27-28) ndipo zitoliro zimagwiritsidwa ntchito pakati pa anthu a Mulungu pofuna kupereka zizindikiro komanso

“Zida

sizimagwiritsidwa

ntchito kwambiri

pa nthawi ya

chipembedzo

kufikira pa nthawi

ya Davide, ndipo

kenaka Malemba

amanenanso kuti

izi zinali monga

inanenera kapena

kulamulira mfumu.”

kuwaitanira anthu ku kupembedza. Saulo anakumana ndi gulu la aneneri amene amaimba ndi zida zosiyanasiyana akuchokera ku mapiri (1 Samuele 10:5). Mneneri Elisa anaitanitsa woimba lingaka kuti amuimbire (pofuna kuti mtima wake utsike) asanayambe kunenera motsogozedwa ndi Ambuye. (2 Mafumu 3:14-15). Pamene zida zoimbira zimagwiritsidwa ntchito, nkofunika kuzindikira kuti sizimagwiritsidwa ntchito mu kupembedza kwa mu *chihema chokomanako*. Ngakhale kuti Mulungu adapereka tsatanetsatane wa mmene amayenera kumangira chihema chokomanako, zinthu zokhala mmenemo, kaperekedwe ka nsembe ndi kapembedzedwe, zida zoimbira sizimagwira ntchito pa nthawi ya chipembedzo.

Davide—Wokonda maimbidwe

Mfumu Davide, ngakhale akadali wamng'ono, anali katswiri poimba zeze. Pamene Mfumu Saulo anasautsidwa ndi mzimu woipa, Davide amamuimbira zeze, ndipo mtima wa Saulo umabwerera mchimake, ndipo mzimu woipawo umamusiya (1 Samuele 16:15-23). Uwu ndi umboni wa mphamvu ya maimbidwe. Maimbidwe akhoza kukhudza mtima wa munthu koposa mmene angachitire mau. Ngakhale kuti kugwiritsa ntchito zida zoimbira kukhoza kuchotsa mavuto ndi nkhwaza za m'maganizo, zimakhala za kuthupi ndipo sizingabweretse kusintha kwamuyaya.

Davide anali munthu amene amakonda maimbidwe ndiponso zida zoimbira. Pamene likasa la chipangano limanyamulidwa, iwo anachita zimenezo monga “Mose anawauza, monga mwa mau a Yehova” (1 Mbiri 15:15-16); koma ngakhale izi zinali choncho, Davide analamulira mkulu woyang'anira Alevi kuti asankhe anthu akuti adziimba pogwiritsa ntchito zida zoimbira. Ngati kuti izizi sanalamulire ndi Mulungu, chinali chitsimikizo chakuti mtima wa Davide unatsamira pa za maimbidwe. Nyimbo za Masalmo ndi zodzaza ndi mayamiko ndipo zimaonetsera kugwiritsa ntchito zida zoimbira potamanda Ambuye (Masalmo 150:1-6). “Mumuimbire Iye nyimbo yatsopano; muimbe mwaluso kumveketsa mau” (Masalmo 33:3).

Mfumu Davide anakhazikitsa zida zoimbira

Mfumu Davide inapanga zida zoimbira za mu nyumba ya Mulungu (1 Mbiri 23:5). Ngakhale kuti zidazo sizimagwira ntchito mu *chihema chokomanako*, Malemba atitsimikizira kuti anthu oimba mau chabe ndi oimba zida amasankhidwa kuti atumikire chipembedzo cha mu *kachisi* monga “anawalangiza ndi mfumu” (1 Mbiri 25:6). Alevi anaikidwa mu kachisi ndi zida zoimbira “monga umo adauzira Davide” ndipo zinali “zoimbira za Davideyo mfumu ya Israele.” (2 Mbiri 29:25-28). Kachisi wa Solomoni ataonongedwa, ndipo pamene kachisi watsopano amamangidwa anthu atabwerako ku ukapolo wa ku Babiloni, pa Ezara 3:10 akunena za Alevi kuti anagwiritsa ntchito zida zoimbira polemekeza Yehova “monga umo anaikiratu Davide mfumu ya Israele.” Ngakhale kuti kupembedza pa nthawiyi kunali kwa mwambo osati kwa uzimu, nkofunika kuzindikira, ndi kudziwa bwino lomwe, kuti zida zoimbira sizimagwiritsidwa ntchito mu chipembedzo mpaka kufika nthawi ya Davide, ndipo



Malemba amanena momveka bwino lomwe kuti zinaikidwa kapena kulamulidwa ndi mfumuyo.

Uneneri wolengeza za tsoka

Mneneri Yesaya analengeza tsoka pa iwo amene anali ndi chibaba cha chakumwa chaukali, nadyerera ndi kuimbira zida pa maphwando awo koma osalabadirako Ambuye. Mneneri Amosi anawadzudzula anthu a Mulungu momveka bwino kuti: “Tsoka osalabadirawo m’Ziyoni, ndi iwo okhazikika m’phiri la Samariya.... akungoimba kutsata maliridwe a zeze, nadzilingiririra zoimbira nazo ngati Davide;” (Amosi 6:1-5). Mulungu anada kukhosi ndi masiku a maphwando ndipo samalandiranso nsembe zao. “Mundichotsere phokoso la nyimbo zanu; sindifuna kumva maimbidwe a zisakasa zanu.” (Amosi 5:21-24). Ngakhale kuti zida zoimbira za Davide zimatulutsa mingoli yokoma ndi yanthetemya imene imatha kukhudza ndi kuthuzitsa mitima ya anthu, komabe izi sizinakwanitse kuwabweretsa ana a Israele mu ubale wauzimu ndi Mulungu. Wolemba wina anafunsa funso kuti: “Ngati zopanga munthu zinakanika kubweretsa zipatso za uzimu pansi pa lamulo lakale, tsono tingayembekeze kuti izo zikhoza kubweretsa chauzimu ngakhale mu nyengo yatsopanoyi?”

Pangano latsopano libweretsa kupembedza kwauzimu


Lamulo linakwaniritsidwa (Mateyu 5:17) ndipo njira ya chiyero ndi choonadi chenicheni inapezeka mwa Khristu. Pangano loyamba lija linachotsedwa kuti potero Khristu “akhazikitse lachiwirilo” (Ahebri 10:1-9) ndi kukonzanso izo zimene lamulo silimakwanitsa kuchita. Moyo watsopanowu mwa Khristu unasinthiratu machitidwe ndi kupembedza kwa tsiku ndi tsiku kwa ana a Mulungu enieni. Zolamulira za kupembedza kwa thupi sizinakhazikitsidwe pa anthu koma panali chiyanjano chotimasula, chauzimu ndi chosatchingidwa ndi zinthu za thupi. Paulo analalikira kwa a ku Atene pa phiri la mulungu wao Mars ndipo molimba mtima analengeza kuti Mulungu “sakhala m’nyumba za kachisi zomangidwa ndi manja; satumikiridwa ndi manja a anthu, monga wosowa kanthu” (Machitidwe 17:22-25). Mulungu samapembedzedwa kapena kulemekezidwa ndi ntchito kapena luso la manja a anthu ndiponso samakhala mu akachisi okongola amene anamumangira kapena kumangira milungu yabodza. Mulungu ndi mzimu ndipo amapembedzedwa moonadi ndi iwo amene Iye anawapatsa moyo ndi mpweya. Munthu anabwera wachikwanekwane kuti apembedze Mulungu ndipo safunikanso china choonjezera

kuposera moyo ndi mpweya kuti adzipereke yekha ngati chida cha chilungamo.

Thupi ndi mzimu

Kupembedza mu Chipangano Chakale kunali kwa thupi ndi koonekera, koma tsopano kupembedza kooni ndi kovomerezeka ndiko kwa Mzimu. Kupembedza kwenikweni kwa uzimu kumalamulira zochotseratu kupembedza kwathupi kopereka nsembe, kufukiza libano ndi zina, komanso nyimbo zochokera ku zida zopanda moyo. Malemba a mu Chipangano Chatsopano akunena za njira yatsopano ndi yabwino kwambiri ya kupembedza ndipo chitsanzo chake chinaonetsedwa mwa Khristu ndiponso mpingo woyambirira. Atatha kudya phandwo la Paska, Yesu ndi ophunzira ake “anaimba nyimbo” (Mateyu 26:30). Zida za Yubala ndi Davide zapita kwawo ndipo zilibenso ntchito mu mpingo wa Chipangano Chatsopano. Masiku ano Mulungu sapembedzedwa ndi mau ochokera ku zida zochita kupangidwa, koma amapembedzedwa mu kukongola kwa chiyero chenicheni — izo zimene luso la munthu silingatse kuzipanga. Pa Aroma 15:9 akunena kuti “ndidzaimbira dzina lanu.” Paulo akulangiza mpingo wa ku Korinto kuti uimbe ndi mzimu komanso uimbe ndi chidziwitso (1 Akorinto 14:15). Palibe kuzindikira kulikonse mu mau omveka kuchokera ku zida koma awo ochokera mu mtima ndi pakamwa amalungamitsidwa. Mpingo woyamba sunalangizidwe kuti udzigwiritsa ntchito zida pofuna kulemekeza Ambuye; komabe iwo amauzidwa mobwerezabwereza kuti “imbirani” (Ahebri 2:12). “Ndi kudzilankhulira nokha ndi masalmo, ndi mayamiko, ndi nyimbo zauzimu, kuimbira ndi kuimba m’malimba Ambuye mumtima mwanu” (Aefeso 5:19). Akolose amalimbikitsidwa kuphunzitsana ndi kulangizidwa wina ndi mnzake mu “masalmo, ndi mayamiko ndi nyimbo zauzimu, ndi kuimbira Mulungu ndi chisomo mumtima mwanu.” (Akolose 3:16).

“Ngati zolenga za munthu zakanika kubweretsa zipatso za uzimu pansi pa lamulo lakale, tsono nanga tingaliyembekeze bwanji kuti likabweretsa chauzimu pansi pa nyengo yatsopanoyi?”



(Yapitirira pa tsamba 8)

(Kuchokera pa tsamba 7)

Kuimbira pakamwa kokha kukulimbikitsidwa mu Chipangano Chatsopano

Chipangano Chatsopano sichiletseratu kugwiritsa ntchito zida zoimbira pa nthawi ya chipembedzo, koma kuti palibe kuloleza komveka bwino kuti tizigwiritsa ntchito zida zoimbira monga mmene palibe chilolezo chomveka chakuti tidzifukiza kapena kuyatsa makandulo. Kusiyanana kwa chiphunzitso pakati pa Chipangano Chakale ndi Chatsopano ndi koonekeratu, ndipo sitinganene kuti pali kuloleza pa chinthu chimene sichinaperekedwe mpoyamba pomwe. Mau a Mulungu sakunena kalikonse za kugwiritsa ntchito zida zoimbira mu Chipangano Chatsopano, komanso akulangiza oyera mtima onse kuti aimbe ndi kuthira mang'ombe m'mitima mwao. Iye tiyenera kuti “tipereke chiperekere nsembe yakuyamika Mulungu, ndiyo chipatso cha milomo yovomereza dzina lake” (Ahebri 13:15). Kuimba kogwiritsa ntchito mau basi ndi maimbidwe okhawo amene ali ovomerezeka ndi Mulungu mu Chipembedzo cha Chikhristu.

Zikhalidwe za mu Mpingo woyamba



Mbiri imatiuza kuti Mpingo Woyambirira amapembedza poimba nyimbo monga mmene anaphunzirira M'malemba ndipo sanagwiritsa ntchito zida zoimbira. Taganizirani za izi zimene zinalembedwa:

“Kugwiritsa ntchito nyimbo sikunalandiridwe m'mpingo ya Chikhristu, monga mmene zinaliri pakati pa Ayuda, panthawi imene mpingo unali usanakule, ndipo amangogwiritsa ntchito nyimbo basi” (Justin Martyr. A.D. 139).

“Chida chimodzi cha mtendere, Mau basi amene tilemekeza nawo Mulungu, ndi zimene tilimbikitsa. Sitilimbikitsa Salmo lakale, ndi lipenga, ndi lingaka ndi chitoliro” (Clement of Alexandria. A.D. 153-217).

“Zionetsero za maimbidwe ogwiritsa ntchito magitala ndi zitoliro ndi za milungu yakale ngati Apolo, Muses, Minerva ndi Mercury imene inapanga zimenezi; inu amene muli Akhristu, mudane ndi kunyansidwa nazo zinthu izi zimene ngakhale kwa ozipangawo zimakhala zinthu zodedwa ndi zosocheretsa” (Tertullian. c. A.D. 200).

“Zida si za iwo amene ali Akhristu” (John Chrysostom. A.D. 345-407).

“Maimbidwe mu ma tchalichi ndi chinthu chakale kwambiri monga mmene aliri atumwi, koma kuimba kogwiritsa ntchito za sikwakale choncho.” (Joseph Bingham. *Works*. Vol. III, p. 137).

“Palibenso kukayikira kuti poyambirira kwina kulikonseko maimbidwe a kupembedza wakumwambayo anali a mau a pakamwa basi.” (Emil Nauman. *The History of Music*. Vol. I, p. 177).

“Akhristu nawonso amakhazikika pa mfundo yomweyi, monga mmene tikudziwira kuchokera ku zolembe za nthawi ya atumwi komanso m'zaka za patsogolo: nyimbo zoimbira zida zimaganiziridwa kuti ndi zosayenera pa miyambo ya chipembedzo; mabuku ena a Chikhristu amanena momveka bwino ndi mosapsatira podzudzula mchitidwe woimbira zida. Poyambirira, nyimbo zokha zimaganiziridwa kuti ndiye njira yeniyeni pofuna kulumikizirana ndi Mulungu” (*New Oxford History of Music*. Vol I, p. 135).

“Kuimba kokha basi, osati kuimba zida kumaloledwa mu mpingo woyamba” (Hugo Leichtentritt).

“Nyimbo zimene amagwiritsa ntchito, zinautsa mzimu wa kupembedza kwao — kufatsa kwamkati. Nyimbo zonse zimene zinaimbidwa mu zipembedzo zonse zinali zoimbira pakamwa” (F. L. Humphrey. *Evolution of Church Music*).

“SINDITSUTSANA NDI ZIDA ZOIMBIRA MU MATCHALICHI ATHU
POKHAPOKHA BOLANI ZISAONEKE KAPENA KUMVEKA.”
— JOHN WESLEY (1703-1791)

Chiyambi cha zida zoimbira mu Mpingo wa Katokila

Kugwiritsa ntchito zida zoimbira sikunayambirensa mpaka m'zaka za m'ma 600 ndi 700 AD pamene zida zoimbira zinayambiranso mu mpingo wa Katolika ngakhale mocheperapo. Panali anthu ochuluka amene amasutsana ndi kugwiritsa ntchito zida zoimbira mwakuti pa msonkhano wao waukulu wotchedwa Council of Trent (1545) anatsala pang'ono kuziletsa kugwiritsa ntchito kwake (*Schaff-Herzog Encyclopedia*, II, 1702). Patapita zaka zingapo, ambiri mwa anthu a Chiprotestant amene anakonzanso mpingo sanagwiritse ntchito zida zoimbira mu chipembedzo. Ngakhale zimaoneka ngati zachilendo kwa anthu alero kuimba ndi pakamwa pokha basi kuimba (a capella), kwa zaka zambiri, mpingo yambiri yaikulu yakhala ikuphunzitsa kuti kugwiritsa ntchito zida zoimbira mu chipembedzo sikoyenera.

Mpingo wamakono ulola kugwiritsa ntchito zida zoimbira

Ngakhale posachedwapa, mu zaka za m'ma 1800, atsogoleri ambiri a Mipingo amakaniza kugwiritsa ntchito zida zoimbira mu mwambo wa chipembedzo pokhulupirira kuti zinali zosayenera pa kupembedza kwa zauzimu. Nkhondo ya pa chiweniweni yaku United States itatha m'chaka cha 1865, mbusa wina, Benjamin Franklin, ananena kuti panali matchalichi okwana pafupifupi 10,000 ku Amerika koma mwa onsewo matchalichi osakwana 50 amagwiritsa ntchito zida zoimbira pa nthawi ya chipembedzo. Mchitidwe uwu wogwiritsa ntchito zoimbira umene wafala masiku ano unali usanafale panthawi imeneyo. Matchalichi akuoneka kuti akukondweretsedwa ndi kufuna kupeza anthu ochuluka ndiponso kutumikira

(Yapitirira pa tsamba 10)



KUCHOKERA KWA OKONZANSO MPINGO...

“ORGAN MU CHIPEMBEDZO NDI CHIZINDIKIRO CHA BAALA. AKATOLIKA ANABWEREKA IZI KUCHOKERA KWA AYUDA.”

—MARTIN LUTHER (1483-1546)

“Zida zoimbira pokondwerera matamando a kwa Mulungu sizingakhale zabwino kuposa kufukiza nsembe, kuyatsa makandulo, ndi kubwezeretsanso zithunzithunzi za malamulo. Akatolika, mwakusadziwa ndi mopusa abwerekera izi, komanso zinthu zina, kuchokera kwa Ayuda. Anthu amene amakonda zokometsera zakunja akhoza kusangalala ndi phokosolo, koma zophweka zimene Mulungu akufuna kuti ife tichite kudzera mwa atomwi ndi zomukondweretsa lye kwambiri.”

— John Calvin (1509-1564)
Commentary on the 33rd Psalm

**“[D.S. WARNER]
ANAPHUNZITSA
MOMVEKA BWINO
NDIPO MWAMPHAMVU
ANATSUTSANA NDI
KUGWIRITSA NTCHITO ZIDA
ZOIMBIRA PA KUPEMBEDZA
MULUNGU. PALIBE IMODZI
MWA MPINGO [YA
CHURCH OF GOD] IMENE
INAZIGWIRITSA NTCHITO MU
NTHAWI YA MOYO WAKE.”**

**—C. E. ORR (1844-1933)
NOT A NEW MOVEMENT**

“Ine [kupitirira apo] ndikhulupirira kuti kugwiritsa ntchito zida zotere pa maimbidwe, mu mpingo wa Chikhristu, ndi kuchita opanda chilolezo komanso motsutsana ndi chifuniro cha Mulungu; iwo akugalukira mzimu wa kudzipereka kwathunthu ndipo akuchimwa... Ndine nkhalamba tsopano, ndipo ndine mbusa wokalama, ndipo ndikunenetsa kuti sindinaonepo iwo amene anachita zabwino popembedza Mulungu; nakhala ndi maganizo akuti iwo amachita zoipa zochuluka. Maimbidwe ali ngati maphunziro, ndipo ndimawalemekeza ndi kuwasirira, koma kugwiritsa ntchito zida mu nyumba ya Mulungu, ndimadana nazo ndi kunyansidwa nazo. Kumeneku ndi kuononga maimbidwe, ndipo ndikunena kuti sindigwirizana ndi zonse zopotoza kupembedza kwa lye amene anayamba Chikhristu.”

—Adam Clarke (1762-1832)
Commentary on Amos 6:5

(Kuchokera pa tsamba 9)

thupi osati mzimu. Kulekerera kotereku kunayamba pamene matchalichi anayamba kugwiritsa ntchito organ ndi piano ndipo pano zafalikira kufika ku ma bandi ndi magulu oimba ogwiritsa ntchito zida zosiyanasiyana. Maimbidwe a dziko akhalanso maimbidwe a mpingo walero. Mchitidwe wamasiku ano wolemekeza ndi kulambira pogwiritsa ntchito zida ndi wa kuthupi. Pamene zida zoimbira zikhoza kupereka chikoka ku zimene munthu amamva m'thupi mwake ndi kwa mzimu wa munthu, mphamvu yake ndi ya kuthupi ndipo si gawo la chipembedzo chenicheni cha uzimu.

Kupembedza kwauzimu kukufunikira

Posatengera kuti miyambo ndi zikhalidwe ndi zosiyana motani, kaya kuimba ng'oma kumene kumachitika ku Africa, ndi kuimba limba ku Asia, ndi ma orchestra a ku Europe, komanso ma bandi a ku America, njira yosavuta yopembedza mwauzimu isapose zimene chikhalidwe chimachita kapena kuvomereza. Mapembedzedwe awa a thupi ndi a dziko ndipo amakhazikika pa chilakolako cha thupi ndi chilakolako cha maso, matamandidwe a moyo (1 Yohane 2:15-17). Mipingo yambiri, pokonda dziko lapansi, asiya njira yosavuta imene inaphunzitsidwa M'malemba ndipo chitsanzo chake chinaonetsedwa ndi mpingo woyambayamba. Mtumwi Paulo anachenjeza Timoteo kuti m'masiku otsiriza “zidzafika

nthawi zowawitsa. Pakuti anthu adzakhalaokonda zokondweretsa munthu, osati okonda Mulungu; akukhala nao maonekedwe a chipembedzo, koma mphamvu yake adaikana; kwa iwonso udzipatule” (2 Timoteo 3:1-5).

Kupembedza kotsogozedwa ndi Mzimu Woyera

Kufikira lero, anthu a Mulungu akuitanidwabe kuti alole kuti miyoyo yao ikhale yoyera, ndi nsembe zamoyo. “Ndipo musafanizidwe ndi makhalidwe a pansi pano: koma mukhale osandulika, mwa kukonzanso kwa mtima wanu, kuti mukazindikire chimene chili chifuno cha Mulungu, chabwino, ndi chokondweretsa, ndi changwiro” (Aroma 12:1-2). Kupembedza kwa uzimu si kusapezeka kwa zida zoimbira kokha, koma kupezeka kwa Mzimu Woyera akuyenderera kuchokera mu moyo wachiyero. Tilole kuti mizimu yathu ilumikizane ndi maimbidwe akumwamba ndipo chiyanjano chiyenderere kuchokera ku mitima imene ili yodzaza ndi chisomo cha Mulungu. Tiyeni nthawi zonse tikhale miyala yamoyo, nyumba ya Mulungu ndiponso ansembe achifumu amene akupereka nsembe zauzimu zimene zili zovomerezeka kwa Mulungu mwa Yesu Khristu (1 Petro 2:5).

—mws

Malangizo kuchokera mu Baibulo

Pembedzani mu Mzimu ndi mu Choonadi. —Yohane 4:23-24


Dzilankhulireni nokha mu Nyimbo. —Aefeso 5:19

Phunzitsani ndi Kulangizana wina ndi mnzake. —Akolose 3:16

Imbani ndi Chisomo mu Mtima mwanu. —Akolose 3:16

Imbani ndi Mzimu ndi Chidziwitso. —1 Akorinto 14:15

Imbani ndi Malimba mu mtima mwanu. —Aefeso 5:19





Kodi ndi kulakwa kugwiritsa ntchito zida zoimbira pa nthawi ya chipembedzo?

Kugwiritsa ntchito zida zoimbira pakokha sikolakwa ai, koma malingana ndi malemba ndiponso mbiri ya mpingo, kugwiritsa ntchito zida zoimbira mu chipembedzo si njira yoyenera ndi yovomerezeka pakulambira Mulungu. Tiyanera kusamala kuti tisaweruze aliyense amene amagwiritsa ntchito zida ngati iye ndi olakwa chifukwa anthu akhoza kukhala ndi chidziwitso komanso mapenyedwe osiyana pa mutuwu. Pali zinthu zina zimene sitinganeneretu kuti ndi uchimo kapena ayi, koma cholinga cha moyo uliwonse oona mtima ndicho chakuti atsatiye Ambuye ndi mtima wao wonse koma monga mmene

angathere. Yakobo 4:17 akunena kuti, “Potero kwa iye amene adziwa kuchita bwino, ndipo sachita, kwa iye kuli tchimo.” Ngati wina wake akudziwa ndiponso kuzindikira choonadi ichi mwa Mzimu, ndipo safuna kusintha chifukwa cha “chikondi cha pa zida,” zikatero umakhala uchimo chifukwa cha kugalukira mtima wake. Kupembedza mu uzimu posagwiritsa ntchito zida zina zilizonse ndiye njira yoposetsa. Iwo amene satsatira njirayi akuchita mosiyana ndi chitsanzo chimene tikuchipeza mu Chipangano Chatsopano ndipo akusemphana ndi madalitso aakulu a kupembedza kwauzimu kwenikweni. —mws

Kodi nchifukwa chiyani sitiyanera kutsatira malamulo a Davide kuti tipembedze Mulungu ndi zida zoimbira, ngakhale kuti Davide anali “munthu wapamtima pake pa Mulungu”?

Malemba onse ayenera kumasuliridwa ndi kuwunikiridwa molingana ndi nyengo yake. Mu Masalmo 144:1, Davide akunena kuti, “Wolemekezeka Yehova thanthwe langa, wakuphunzitsa manja anga achite nkondo, zala zanga zigwirane nao.” Ndi zoona ndithu kuti Mulungu anadalitsa Davide mu nkondo zake pomenyana ndi mitundu ina, ndipo zinamuthandiza iye kuti aphe ndi kugonjetsa adani ake komabe izi ndi zachilendo mu nyengo ino ya Uthenga Wabwino. Panopa Mulungu akufuna kuti tileke nkondo ndi kumenyana, ndi kuti tikonde adani athu, tichite zabwino kwa iwo amene amadana naye ndipo amafuna kutigwiritsa ntchito mwachipongwe, ndi kuti “Musakaniza munthu woipa” (Mateyu 5:38-45). Mulungu analolanso kuti Davide akhale ndi akazi ambiri ndipo anamudalitsa iye komanso ana amene anabadwa kuchokera kwa akazi amenewa. Mu nyengo ino, Mulungu amaudzudzula mchitidwe umenewu ndipo sadzadalitsa munthu aliyense amene angatsatiye chitsanzo ichi cha mitala cha Davide. Nchifukwa chake, Malemba onse amayenera kutanthauziridwa ndi kumasuliridwa molingana ndi nyengo yake. Izi ndi zoona ndithu monga mmene akunenera pa Masalmo 150:3-8 ndi Masalmo ena amene amatilamulira za kugwiritsa ntchito zida zoimbira poimba ndi kuvina pamene tikupembedza Mulungu. Palibe mau a ku Chipangano Chakale amene angafufute chiphunzitso kapena mfundo ya ku Chipangano Chatsopano. Chipangano Chatsopano ndi “chipangano chabwino” ndipo ndi chimene Mulungu amafuna kuti tidzikhazikikapo masiku alero.

Zoonadi, Davide, mu nyengo yake anali “munthu wapamtima pake pa Mulungu.” Komatu iye amene akufuna kukhala wapamtima pake pa Mulungu mu nyengo ino ayenera kukhala m’moyo wodzipatula oposa wa Davide kapenanso umene Davideyo sanaganizireko. —Harlan Sorrell

Mu Aroma 15:9 ndi Yakobo 5:13 mau akuti *imba* akutanthauziridwa kuchokera ku mau a Chigriki akuti *psallo*. Kodi malemba amenewa akunenanso za kugwiritsa ntchito zida zoimbira mu Chipangano Chatsopano?

Ayi, Malemba awa sakulimbikitsa kapena kulangiza za kugwiritsa ntchito zida zoimbira. Kugwiritsa ntchito kwa mau akuti *psallō* kwabweretsa mpungwepungwe chifukwa chakuti tanthauzo la mauwa lakhala likusintha nkupita kwa nthawi. Tanthauzo limodzi, limene tikuliona mu mabuku olongosera mau a mu Chigriki ndilo, “kukodola kapena kuliza” monga mwa kuimba ndi chida chokhala ndi zingwe. Komabe, mabuku a akatswiri a Baibulo ophunzira mozama ndi otchuka amalongosola kuti pamene mauwa agwiritsidwa ntchito mu Chipangano Chatsopano amatanthauza “kuimba.”

Buku la *Thayer’s Greek-English Lexicon of the New Testament* limanena kuti mau a *psallō* mu Chipangano Chatsopano amakamba za “kuimba nyimbo, kukondwerera malemekezo a Mulungu mu nyimbo.” Buku la *Vine’s Expository Dictionary of New Testament Words* nalonso limapereka tanthauzo lakale la *psallō* ndipo kenaka limanena kuti “mu Chipangano Chatsopano, limatanthauza kuimba nyimbo, kuimba zolemekeza.” —mws



KODI MUKUDZIWA?

Ndipo pamene adatenga bukulo, zamoyo zinai ndi akulu makumi awiri mphambu anai zinagwa pansi pamaso pa Mwanawankhosa, zonse zili nao azeze, ndi mbale zagolide zodzala ndi zofukiza, ndizo mapemphero a oyera mtima. —Chivumbulutso 5:8

Buku la Chivumbulutso lili ndi zifanifani zochuluka ndipo limalongosola popereka zinthunzi zokongola za oyera mtima atazungulira mpando wa chifumu ndi azeze m’manja mwao, akuimba nyimbo ya Chipulumutso. Azeze awa kumwambako si azeze enieni koma ndi chithunzithunzi choimira matamando amene akuperekedwa kwa Mulungu. Iwo akuonetsera umodzi ndi mgwirizano umene umabwera chifukwa cha kukhala m’chiyanjano ndi Mzimu.



**Mau a
Nyengo
Yake**

CHUNANI NSAMBO ZANU

Kuti Mutipeze

The Gospel Truth
P. O. Box 2042
Nixa, MO 65714
USA

Email:
editor@thegospeltruth.org

“Chunani nsambo zanu inu chigulu choombedwa, ndipo kwezani Khristuyo.
Imbirani dzina limene litsekula makomo a chifundo;
O, ‘ndi nyimbo, nyimbo zokometsetsa kwa ochimwa otayika,
Zokometsetsa mpaka muyaya kwa oyeramtima.”

—Warner, Daniel. *The Music of His Name*.

Panthawi ya chionetsero, nyimbo isanayambe kuimbidwa, oimba amachuna zida zao kuti zifikire pa mulingo woyenerera kuti potero pakhoza kukhala mgwirizano pamene akuimba. Mau a anthu ndi zida zomwe sangamveke bwino ngati wina aliyense achuna chida chake malinga ndi mmene iye akufunira. Koma akachuna potsatira zimene wotsogolera wawauza, mau ake adzakhala ogwirizana ndi okoma kuwamvera.

Pamene anthu akumana pamodzi kuti apembedze Ambuye, nkofunikira kuti aliyense wa iwo akhale kuti wakonzatima wake ndipo ali mu mzimu umodzi ndi Mzimu Woyera, monga wolembe ananena kuti “chunani nsambo zanu.” Nthawi ya chipembedzo ndi pamene timasiya zopsinje ndi zosamalira za moyo uno kuti tonse pamodzi tilemekeze ndi kuphunzira kuchokera kwa Khristu. Ngati mpingo wasemphana ndi Mzimu, pamenepo padzakhala mau a nyimbo osamveka bwino.

Kulumikizana kwa Mzimu kumachokera mu mitima imene yakonzanso miyoyo yawo kuti ifanane ndi muyeso wa Mbuye wathu. Nkoyenera ndithu kuti nthawi ya chipembedzo ikhale yopindula kuti potero atsogolera a utumiki ndi a zauzimu adzikhuthule kwathunthu ku zolemetsa za moyo ndi kudzikonzekeretsa mitima ndi maganizo awo kuti alumikizane ndi Mzimu Woyera. Pamene izi zakwaniritsidwa, kudzoza kwake kumakhala kolemerera ndipo mpingo umadalitsidwa kwambiri chifukwa cha kuyenda kwa myaa kwa Mzimu Woyera. “Chunani nsambo zanu” kuti chimwemwe cha Ambuye chichulukire mu kutamanda ndi kupembedza kwa Ambuye. —mws



CHIYERO CHA KWA AMBUYE